


MULINGO WA GOLIDE WA MAPHUNZIRO A CHIKHRISTU



Ndipo mchilamulo chake amalingaliramo usana ndi usiku. Iye ali ngati ntengo odzalidwa m'bali mwa mitsinje ya madzi Masalimo 1:2-3

Maphunziro amakono ophunzirira pakhomo amangika papa mfundo zochokera m'buku la **Deutronomo 6:4-9**, ndime imeney imatsimindika kuti makolo ali ndi udindo ophunzitsa ana awo, maphunziro amenewa ayenera kugwirizana ndi mitu komaso zochitika za masiku athu ano (**Deutronomo 6:7, luka 24:27 kuti kaonekedwe ka zomwe aphunzira**)

Ndime imeneyi imadziwika ngati lamulo loyamba **Marko 12:32-33, luka10:27**. Ngakhale kuti ena mwa akhristu samakhulupirira mfundo yokhudza malamulo khumi kuti ndi ofunika komaso akugwira ntchito kufikira lero, chithunzi chili pamwambachichi chikuonetsera kuti malamulo khumi aja ndi mulingo osasintha pa zinthu zofunika kwambiri za moyo. Ndipo mauwa akuchitabe mpaka tsopano.

Baibulo limatiuza kuti magome awiri a malamulo aja amaimirira kukonda Mulungu ndi kukonda nzako monga udzikonda mwini (**Aroma 13:9 Mateyu22:40, Ijohn 3:23**).

Magulu ambiri achikhristu amati malamulo anayi oyambirira a malamulo khumi amakamba zokonda Mulungu. Ndipo amaika asanu ndi awiri otsiriza kuti amakamba za kukondana wina ndi mzake. Malingaliro amakamba za kugawa malamulo khumi anayi komaso asanu ndi awiri kuti ali opatulika komaso ena osakhala achikhristu kuti anthu awagwiritse ntchito. Zina mwa zotsatira za kagawidwe ka 4 kuphatikiza 6 ka malamulo khumi ndi kakuti khoti yaikulu mu dziko la amereka anatanthauziraso kuti tanthauzo la ukwati kuti uli mmanja mwao kutero. Ndi chinthu chodziwika bwino kuti uta waleza umatikumbutsa za chifundo cha Mulungu kwa anthu a mitundu yose (Genesis 9-13-16). Ndipo tsopano zikuonetrsera chizindikiro cha chilolezo cha maganizo aja a (umodzi mu ukwati)

Akhristu ena amati malamulo khumi anali a anthu a nthawi imeneyo. Kaganizidwe kotere kamapangitsa akhristo ambiri kukhala osakhwima mu uzimu (**Aheberi 5:12-14**)

Mongofananiza maganizidwe onsewa **chiphunzitso cha paphiri ku mateyu 5-7** akunena kutimalamulo anayi oyambirira aja ali ngati mizu (kuyambira lamulo 1-5) ndipo malamulo 6-10 ngati zipatso (Eksodo20, Deutronomo 5)ndondomeko yonse yaikidwa bwino m'buku la Mateyu5-7 komaso m'buku la Yakobo. Mwachitsanzo **Kupembedza ma fano** (lamulo la chiwiri) lamulo ili limadziwika ngati kuchita chigololo (lamulo la seveni, yakobo4:4 hoseya 1:2). Mzimu olemba lamulo lachiwiri ndi lachisanu ndichiwiri akuoneetsera chiyanjano, kudzikhutura ndi kudzipereka. Mwandondomeko yake lamulo lililose pa gome loyamba lija lili ndi



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

chipatso pa gome lachiwili lija. Mizu inayenera kukhazikitsidwa pasanabwere chipatso (mateyu5:15-20, yakobo 2:26).

Mwachidule palibe chomwe tingachite wopanda khristu, yemwe ndi mpesa (yohane 15:4,5) Timatumikira Kristu mu moyo watsopano osati mukalata ya kale ija (Aroma 7:6).

Cholinga cha izi ndi kuvumbulutsa malamulo khumi mizu yake komaso zipatso zake ngati mulingo wa golide mu chipangano chakal;e komaso chatsopano, monga momwe Yesu ananena ku Yohane5:46 komaso Mateyu22:40, Pamalamulo awiri awa pakolekeka chilamulo chonse ndi aneneri. **Ngati simunganvetsetse mfundo zalembedwa mmusimuzi werenganiso chiphuzitso cha paphiri cha pa mateyu 5-7 pomwe zafotokozeredwabwino.**

Mitu imene ikupezeka m'buku la mateyu pa chiphuzitso cha paphiri ndi buku la yakobo ndi yofunika kwambiri mu zochitika za umoyo wa chikristu. Mitu imeneyi ikuonetsara kupita patsogolo komaso zinthu zosaiwalika pa kuphunzitsa ana ndi akulu omwe, tsamba lotsiriza likuonetsera ma vesi ochulika omwe amakamba za kagwiritsidwe ntchito ka malamulo khumi mizu komaso zipatso. Potsiriza pa kufupikitsa nkhanayi fundo izi zikhala zitaonetsedwa bwino.

MALUSO AMOYO ASANU KUCHOKERA KWA YESU KOMANSO YAKOBO

1. **Kubadwanso, kuombedwa ndi kuknhululukidwa**
2. **Ubatizo, ukwati ndi ubale ochita malonda**
3. **Mphatso ndi udindo**
4. **chikhulupiriro ndi ntchito**
5. **kupereka ndi kulera ana**

Mundondo meko ya mizu ndi zipatso siikuonetsa bwino zotsatira za chiphuzitso cha paphiri, koma kuvumbulutsa mdandanda wa ziwiriziwire za mizu ndi zipatso.

1. **Kubadwanso, kuombedwa ndi kuknhululukidwa:** Yesu anayamba ndi kulongosola lamulo la chisanu ndi chimodzi kulifanizira ndi loyamba: pakuti taombedwa (lamulo loyamba), tayenera kukhululukira (lamulo la chisanu ndi chimodzi) [mateyu 5:21-26 fanizo la kapolo osakhululukika (mateyu 18:21-35) James 5:19-20.
2. **Ubatizo, ukwati ndi ubale ochita malonda:** Yesu akuonetsera kusakhulupirika kwa kuthupi (lamulo la chusanu ndi chiwirikwazikika mu kusakhulupirika mu uzumu (lamulo lachiwiri) [mateyu 5:27-30, Yakobo4:4, hoseya 1:2]
3. **Mphatso ndi udindo:** Yesu akuonetsera kuti ngati titatenga zinthu zomwe sizathu koma zili za Ambuye Mulungu, tikatero tili nkuba,(lamulo la chisanu ndi chitatu)ndipo tikatero tili kutchula dzina la Yehova pachabe (lamulo lachitatu) [mateyu 5:31-48] fanizo la oyang'anira mmunda (mathew21:33-45 ndi kapolo okhupirika (mathew 24:45 -51) Psalm 24:1, Yakobo 4:13-17, Miyambo 30:8,9] Fanizo la ma talente (Mateyu 25:16-25, Luka 19:11-27
4. **chikhulupiriro ndi ntchito:** Yesu akufotolozere zokhudza chinyengo (lamulo la chisanu ndi chinayi) chinyengo chimachitika pomwe ife tili kuyang,ana za maonekedwe a kunja kokha, kapena pomwe tiyang,ana pa zinthu zosakhalitsa kuyelekeza ndi za uzimu zomwe liri za muyaya (za tsiku la sabata kapena kuti Lamulo la chinayi) mateyu6:1-18, yakobo 2 Isamueli 16:7 Yesaya 31:1-3.
5. **kupereka ndi kulera ana:** pomwe Ambuye ndi m'busa wathu (Masalimo 23) kapena Tate wathu [mateyu7:11] (lamulo la chisanu) sitimasowa kanthu lamulo la khumi (mateyu6:19-7:11 yakobo 5:7-11.



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

palinso ndime zina za mafanizo zomwe zalimbedwa mu ndondomeko yake yomweyi ya mizu ndi zipatso., kuphatikizapo Fanizo la ofesa lomwe tikikambirane pambuyo pache, kodi nanga fanizo la anamwali khumi ena ochenjera ena opusa aja ali mu gulu liti pa khani ya mizu ndi zipatso, kumbukirani kuti ubatizo Aroma 6:4 ukufanizidwa ndi ukwati mu Aroma 7:1 monga mome lamulo lachiwiri likulumikizana ndi lamulo la chisanu ndi chiwiri, kuti ali malamulo okamba za malonjezano komaso kudzipereka kwathunthu.

Buku la yakobo limaonetseraziwiriziwiri za mizu ndi zipatso munjira yomweyo monga momwe chiphuzitso chapaphiri chimaonetsera, Ndime ziri musizi zikufananitsa chiphuzitso cha paphiri ndi zomwe Yakobo analemba ngati ndondo meko ya mizu komaso zipatso.

Lamulo 6 kulumikizana ndi lamulo 1 m'buku la Mateyu komaso Yakobo

chifukwa choti takhululukidwa (lamulo 1) tayenera kukhululukira (lamulo 6) uwu ndi uwiri oyamba wa Mizu ndi Zipatso wa malamulo khumi

Yesu akufotokozera chiyanjantso chathu ndi abale (muzu wa uzimu) umaposa kupereka mphatso pa guwa **mateyu 5:22-23**

Chomwechoso Yakobo akutsimikiza kufunikira kowaombola abale amene akuphophonya mu chikhulupirilo ngati wina wainu aphonyetsa mu choonadi,

Abale anga, ngati wina wa inu asochera posiyana ndi choonadi, ndipo ambweza iye mnzake; 20azindikire, kuti iye amene abweza wochimwa kunjira yake yosochera adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzavundikira machimo aunyanji. Yakobo 5:19-20

Udani upikisanitsa; koma chikondi chikwirira zolakwa zonse. Miyambo 10:12

lamulo 7 kulumikizana ndi lamulo 2 m'buku la Mateyu komaso Yakobo

Yakobo4:4 akumanga pamodzi lamulo 7 ndi lamulo 2, *Akazi achigololo inu, kodi simudziwa kuti ubwenzi wa dziko lapansi uli udani ndi Mulungu? Poto, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu. Yesu anachita chimodzimodzi poyamba kuonetsera chigplolo cha kuthupi namalizira kuonetsera chigololo cha kuuzimu (kuonongeka kukuonetsedwa mu Mateyu 5:2930, Hoseya 1:2 komaso Yesaya 31:1-3)*

lamulo 8 kulumikizana ndi lamulo 3 m'buku la Mateyu komaso Yakobo

Ngati tatenga zinthu zomwe sizili zathu koma zili za zmbuye tili nkuba, (lamulo 8) ndipo lilitchula Dzina lake pachabe (lamulo 3) miyambo 30:8,9

yesu akuonetsera momwe timatengera zomwe si zathu pa ku lumbira (kulonjeza)

*Ndiponso, munamva kuti kunanenedwa kwa iwo akale, Usalumbire konama, koma udzapereka kwa Ambuye zolumbira zako: 34koma Ine ndinena kwa inu, Musalumbire konse, kapena kutchula Kumwamba, **kutenga za humwanba** chifukwa kuli chimpando cha Mulungu; 35kapena kutchula dziko lapansi, **kutenga za padziko lapansi Masalimo 24:1** chifukwa lili popondapo mapazi ake; kapena kutchula Yerusalemu, **kutenga za ku Yelusalemu** chifukwa kuli mzinda wa Mfumu yaikulukulu. 36Kapena usalumbire kumutu wako, chifukwa sungathe kuliyeretsa mbuu kapena kulidetsa bii tsitsi limodzi. Mateyu 5:33-36*

Yakobo akuperekanso chenjezo lomwelo lokhudza malumbiro

Koma makamaka, abale anga, musalumbire, kungakhale kutchula kumwamba kapena dziko, kapena lumbiro lina lililonse; koma inde wanu akhale inde, ndi iai wanu akhale iai; kuti mungagwe m'chiweruziro Yakobo 5:12 Yakobo akumanga Pamodzi (lamulo 8) usaphe komaso (lamulo 3) usatchule dzina la Yehova pachabe. Pomwe talephera kuzindikira umwini ndi ulamuliro omwe Mulungu ali nao pa zithu, timakhala kuti tikumubera komaso



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

kusalingilira mphanvu zake. Nanga tsono, inu akunena, Lero kapena mawa tidzapita kulowa kumudzi wakutiwakuti, ndipo tidzagonerako ndi kutsatsa malonda, ndi kupindula nao; 14inu amene simudziwa chimene chidzagwa mawa. Moyo wanu uli wotani? Pakuti muli utsi, wakuonekera kanthawi, ndi pamenepo ukanganuka.

15 Mukadanena inu, Akalola Ambuye, ndipo tikakhala ndi moyo, tidzachita kakutikakuti. 16Koma tsopano mudzitamandira m'kudzikuza kwanu; kudzitamandira kulikonse kotero nkoipa. Yakobo4:15-16

Usanyadire zamawa, popeza sudziwa tsiku lina lidzabala chiyani ?

Miyambo 27:1

lamulo 9 kulumikizana ndi lamulo 4 m' buku la Mateyu komaso Yakobo

Yesu akuphuzitsa pa phiri paja kuti chinyengo chimachitika (lamulo 9) tikamayang'ana maonekedwe akunja kwa zinthu kusiya choonadi cha uzimu (lamulo 4 kapena sabata) pali zitsanzo zitatu pa chiphuzitso chapaphiri za chinyengo cha chionetsero cha kunja kwa zinthu mu chiopembedzo

1. kupereka mwa chionetsero
2. kupemphera ndi cholinga choti anthu aone
3. kusala za kudya mwa chionetsero

Yesu akuonetsera kuti choonadi ndi ichi (kapena sabata. Mariko 2:25-26 kuti tizichita mapemphero athu mtseri . Zitsanzo zitatu zija ndi kupemphera mtseri zili zikufananitsa lamulo 4 ndi lamulo 9

Yakobo 2:1-18 akuonetsera kuti anthu amayang'ana za maonekedwe akunja (lamulo 9) pamene Mulungu amaona za muntima (lamulo 4) 1Samueli 16:7. Zomwe yakobo akulankhula zokhudza chikhulupiriro ndi ntchito Yakobo 2:14-26 zikulumikiza choonadi cha uzimu (sabata , lamulo 4) komaso choonadi cha kuthupi (lamulo 9 chipatso). Timanyengeka tikamaganiza kuti kungovomereza ndi pakamwa pokha za chikhulupiriro chathu zimafanana ndi zomwe takhala mu chikhulupiriro chathu.

lamulo 5 kulumikizana ndi lamulo 10 m' buku la Mateyu komaso Yakobo

Ngati yehova ndi m'busa wathu (tate, lamulo 5), pamenepo sitizasowa (lamulo 10) [Masalimo 23.] ichi ndicho chomaliza mu mizu ndi zipatso ya malamulo khumi.

Yesu akutionetsera kuti Ambuye ndiye amatipatsa zosowa zonse ngati kholo lathu lokhala kumwamba.

Kapena munthu ndani wa inu, amene pompempha mwana wake mkate, adzampatsa mwala? 10Kapena pompempha nsomba, adzampatsa iye njoka kodi? 11Chomwecho, ngati inu, muli oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akumpempha lye? Mateyu 7:9-11

chomwechoso Yakobo akufotokozera kufunika kwa kudekha mwa chikhulupiriro komaso chiyembekezo, ndi kukhutitsidwa osa khala adyera. Yakobo 5:1-6

Potero, lezani mtima, abale, kufikira kudza kwake kwa Ambuye. Taonani, wolima munda alindira chipatso chofunikatu cha dziko, ndi kuleza mtima nacho kufikira chikalandira mvula ya chizimalupsa



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

ndi masika. 8Lezani mtima inunso, limbitsani mitima yanu; pakuti kudza kwake kwa Ambuye kuyandikira. 9Musaipidwe wina ndi mnzake, abale, kuti mungaweruzidwe. Taonani, woweruza aima pakhomo. 10Tengani, abale, chitsanzo cha kumva zowawa ndi kuleza mtima, aneneri amene analankhula m'dzina la Ambuye. 11Taonani tiwayesera odala opirirawo; mudamva za chipiriro cha Yobu, ndipo mwaona chitsiriziro cha Ambuye, kuti Ambuye ali wodzala chikondi, ndi wachifundo. Yakobo 5:7-11.

Yesu anaonetsera mu Fanizo la ofesa m'buku la Mateyu 13, ngati chithuzithuzi cha kuonetsera mavuto omwe timakimana nao kuti tifike popeza kholora la uzimu mu ntchito zathu.. ndime imeneyi ikuimiranso mitu yomwe ikupezeka ku Mateyu 5-7, ndipo buku la Yakobo likuonetseredwaso mu Mateyu 13. [chithuzithuzi ichi ndi chofunika kwambiri pa kuphunzitsa ana.](#)

1. **Kubadwanso, kuombedwa ndi kuknhululukidwa [Mbeu za m'bali mwa njira]**
2. **Ubatizo, ukwati ndi ubale ochita malonda [Mbeu za pa minga]**
3. **Mphatso ndi udindo [Mbeu za pa miyara]**
4. **chikhulupiriro ndi ntchito [Mbeu za pa miyara]**
5. **kupereka ndi kulera ana [Mbeu za pa nthaka yabwino]**

Chithu chodabwitsa cha phunziro la ofesa ndi chakuti mitu isanu imeneyi ndizo mitu yomwe mabuku asanu oyambirira a chipangano chakale akufananiza. Ndiposo Mtumwi Paulo akutikumbutsa ku Akorinto 10:1-13

1. **Kubadwanso, kuombedwa ndi kuknhululukidwa [GENESIS, Yosefe akhululukira Genesis50:20]**
2. **Ubatizo, ukwati ndi ubale ochita malonda [EKSODO, Kubatizidwa mwa Mose 1 Akorinto10:2]**
3. **Mphatso ndi udindo [LEVITIKO, Ansembe achifumu 1Petulo 2:9]**
4. **Chikhulupiriro ndi ntchito [NUMER, chivomerezo ndi ntchito ya chikhulupitiro, 1 Akorinto 10:5-13, Aheberi 3,4]**
5. **kupereka ndi kulera ana [DEUTRONOMO, kusamarira ndi kukolola Deut 30:11-20, Galatians 6:7-10]**

Mboni ina ya ndondomeko ya mizu ndi zipatso malamulo khumi yomwe ikupezeka ku Mateyu 22-28, kufanizira malembo [ofiira a chilamulo](#) ndi [obiliwira kuchokera pa Mateyu 22-28.](#)

1. **Maombedwe / kubwezeretsedwa [1,6] zenophobiya [kudana ndi alendo ochora maiko ena] chiyanjano, kukoma ntima, msamaria wa chifundo, ozomoron, kapolo osakhululukira, [uzikonda mzako monga udzikonda mwini Mathew 22:36-40, afalisi ndi aphuzitsi odzitumikira okha Mateyu 23]**
2. **kudzipereka [2,7] kutanthauziranso ukwati, sinkletizimu (kusakaniza zinthu za dziko lapansi) kupaturako kudzipereka, kukhala ndi mkazi m'modzi, kukhulupirika mwa tcheru / anamwali anzeru ndi opusa Mateyu 24: 1-44 fanizo la kapolo okhulupirika Mateyu 24:45-51]**
3. **Mphatso ndi Udindo [3,8] kiulanda zinthu ndi kuchotsetdwa udindo (fanizo la migodi) Fanizo la ma talente Mateyu 25:1-13), kapolo oyipa a m'munda.**



Finding shelter from the Current Social Storms in the two hidden Biblical structures

4. **Kutsimikizika kwa chukhulupiriro/ ntchito, Darwinian naturalism kusankhana mitundu** (Numezi , Mateyu 6:1-18 Yakobo 2:1-13 [kutimikira ochepyedwa kusiyana ndi okwezedwa Mateyu 25:31-46] kuperekedwa kwa Yesu Mateyu 26-27:44
5. **kusamalira ndi ukholo [5,10] kukanidwa kwa Mukungu mbiri ya anthu [Imfa kuikidwa m'manda ndi kuukaso kwa akufa Mateyu 27:44-28:10, kutumidwa kwakukuru Mateyu 28:16-20]**

Magulu awa akutithandiza ndi kuthekera kodziwa kuto mtengo kapena munthu kapena zochitika zima dziwika ndi zipatso ndi khalidwe.

Buku **Zithunzi mmalemba za ulendo wa maomboledwe** pa tsamba lotsatirali komaso pa linki pakuonetsa tchito ya maomboledwe ya Yesu mu mndandanda wa ndime za chipangano cha kale komaso chatsopano. Mitu yaikidwa mu ma kolamu. Cholinga cha chikalata ichi ndi kuonetsera [phunziroli meachidule kuti makolo kapena aphunzitsi athe kuthandiza ena, ma linki ena mu chikalatachi ndi opereka tsatanetsane wa zina pa nkhanayi. Kholora lanu likhale lochuluka.

Mizu ya malamulo khumi Deut5 Mateyu5-7 Yakobo1-5	Zipatza malamulo khumi Deut 5 Mateyu5-7 Yakobo1-5	Mawu pa Aroma 12:1-2	Kufupikitsa mau	Fanizo la ofesa (Mateyu 13:1-23)	Pemphero la Ambuye (Mateyu6:9-13)	Zopereka za a Levi (Ilevitiko 7:37)	Mabuku asanu oyambirira Uthenga wabwino Luka 24:25-27	2 Petulo 1:3-14	Uthenga wabwino wa Yohane chatutala 12-17	Bwalo la kunja kwa chihema
1, kutumikira Mulungu mmodzi umphawi)	6, Usaphe (chifundo) levi 19:34 masalim 103:10-13 aefes 4:32	mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera.	Kudzipereka Kugonjera Aroma 12:1 Aheberi 6:1,2 Afilip 3:9,10	Nthaka yosweka Yer 4:3 Hoseya 10:12 Yoha 12:24 gen 2:7 (mbali mwa njira)	Dzina lanu liyeretsedwe	Nsembe yophysyereza lev 1 Yesaya 53 Lev 6:9-13	Genesis (Yosefe) Yohane 1:1 (Mlengi/Mphungu/muomboli) Aheberi 1:8	(Kutumikira) Chikhulupirilo	Imfa/ Kuukaso kwa Mbeu Yohane 12:24-25	Gome la Mnkwa Imfa ya Nkhosa
1, Usazipangire wekha Fano (chiyero)	7., Usachite chigololo	dipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano	Kuyeretsa Kukonzanso Kukhazikika 1Petulo 3:18-20 Aef 1:13 Aroma 12:2a	Mbeu zabwino Mat 13:38 deut22:9 Gen 3:18 (Nthaka ya minga)	Kufuna kwanu kuchitidwe	Nsembe ya Mbeu Lev 6:14-24	Ekisodo Luka 4:17=25 (Neneri/ Mose) Mat 23:2 Heb 3:1-6 1Akor 10:2	Ukoma	Kuyeretsa mapazi a ophunzira Yohane 13:4-11	Beseni Kuyeretsa kwa thuppi
3, uUsatchule dzina la Yehova pachabe (kusakhulupirika/ umbanda)	8. Usabe	mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu,	Kuphunzitsa Aroma 12:2a Yohane 6:63 1Yohane1:8,9	Nthaka yokonzedwa Yesaya 5:1-7, 12 Nthaka ya miyala	Mutipatse ife lero chakudya chathu chalero Ndipo mutikhululukire mangawa athu	Nsembe ya Uchimo (chifooko) Lev 6:26-39	Levitiko (Aroni) Mark2:17 (Ansembe/Ng'omnbe) 1Pet 2:9 Heb 12:14 2Akor 7:1b 1Pet 1:15-16	Chidziwitso	Kukondana wina ndi mnzake Yohane 13:34-35 Nyumba ... chopimba Yoha 13:37- 141-13	Chihema chokumanamo Efodi, Chofunda choyera
4,Uzikumbukira sabata, (Kukhulupirika / kudalilika)	9.Usachite umboni onama	kuti mukazindiki	Kuyeserera arom 12:2c Aheb 5:14 Aef 5:17,18 Agal5:16 Yere 26:3 Mas 119:97,165	Nyengo ya mayesero (dzuwa) Masalimo 1:3 Yere 17:5,6 1Akori 3:6-9 Nthaka ya miyala	musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo 2Petu 2:7-9	Nsembe yopalamula (cholakwika chachikulu) Lev 7:1-10	Numeri Aheberi 3,4 Ezekiel 1:10	Kudziletsa Chipirilo (Chukhulupiliro cha moyo)	Masautsondi chithonhozo chisamaliri chochokera mu Mpesa Yoha 15:1-17 , 15:18-16:33	Malo ojera choikapo nyali mkate zonunkhira
5, Lemekeza makolo (kunvera, madalitso, kupereka)	10. Usasilire	chimene chili chifuniro cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro.	Chuphuzitso Aheberi 5:11, 6:2 Luke 12:48	Mateyu 13:36-41 Agal6:7-11 2Petu 1:8 Kholora lochuluka	Chifukwa wanu uli ufumu ndi mphanvu ndi ulemelero wanthawi zonse	Nsembe ya Mtendere (kuyamika) Lev 7:11-37	Deutonomo Mateyu 2:2 Mfumu/Mnkango) Aheb 7 Deut17:14-20	Umulungu kukomerana mtima Chikondi Chipatso Chidzalo	Kupembedzera chikhaliidwe cha Kristu Yohane 17:1-26	Malo oyeretsetsa Likasa la Pangano